PHUNZIRO LA 68

1. Kodi anthu anachita chiyani kwa Yesu asanamupachike Iye pa mtanda?
-Anamukwapula Iye.
-Anamunyoza Iye.
-Anamumenya ndikumulavulira Iye.
-Anamumveka nkhata ya minga pa mutu pache.

2. Kodi nkhata ya mingayo inali chizindikiro cha chiyani?
-Nkhata ya mingayo inali chizindikiro cha thembelero la Mulungu.

3. Asilikali aja atamumveka Yesu nkhata ya minga pa mutu pache, kodi chimenechi chinali chizindikiro cha chiyani?
-Chizindikiro chakuti Yesu ndi amene atenge thembelero la Mulungu.

4.Kodi chifukwa chiyani kunali mdima pa dziko lonse kwa ma ora atatu?
-Ma ora atatuwo anali chizindikiro.

5. Kodi chizindikiro chake chinali cha chiyani?
-Mulungu Atate ankamusiya Yesu pa mtanda paja.

6.Kodi chifukwa chiyani Mulungu Atate anamusiya Yesu?
-Mulungu Atate ankapereka chilango kwa Iye chifukwa cha machimo anu, machimo anga, ndi machimo anthu onse.

-Yesu anakhala m'manda usana utatu ndi usiku utatu.

-Kum'mamaŵa, pakutha kwa usana ndi usiku utatu, azimayi ena amene ankakhulupilira kuti Yesu ndi Mulungu

Mpulumutsi anapita ku manda ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:1

1-Ndipo sabata litatha, Mariya wa ku Magadala, ndi Mariya amache a Yakobo pamodzi ndi Salome, anagula zonunkhira kuti akadzodze thupi la Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani azimayi ameneŵa ankapita ku manda a Yesu?
-Ankafuna kuti akalidzodze thupi la Yesu ndi zonunkhira.

-Unali mwambo wa Ayuda odzodza thupi la munthu wakufa zonunkhira asanayikidwe m'manda.

-Chifukwa chakuti Yesu anayikidwa m'manda mufurumira, azimayiwo sanakatha kulidzodza thupi la Yesu ndi zonunkhira.

-Kodi azimayiwo anawona chiyani atafika ku mandako?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:2-4

2-Ndipo pamene ankapita ku manda kum'mamaŵa kwa tsiku loyamba la sabata, dzuŵa litangoturuka kumene,
3-iwo anafunsana kuti, "Kodi ndi ndani amene akatigudumuzire mwala wa pa khomo la manda?"
4-Koma atakweza maso awo, anawona kuti mwala umene unali waukuru uja, wagudumuzidwa.

-Mulungu anatumiza mngero kudzagudumuza mwala otsekera pa manda.

-Kodi azimayiwo anawona chiyani ataloŵa m'mandamo?



-Chifukwa chakuti Yesu anamaliza kale ntchito yopulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Kodi mukuzikumbukira zimene Yesu analankhura kwa mkulu wa amsembe uja, iye atamufunsa kuti Iye anali Kilisitu kapena Iyayi?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:61-62

61-Koma Yesu anakhala chete, osayankha kanthu. Mkulu wa amsembeyo anamufunsanso Iye kuti, " Kodi iwe ndi Kilisitu, Mwana wache wa Odalitsika?"
62-Yesu anayankha kuti, "Ndine amene. Ndipo mudzamuwona Mwana wa Munthu atakhala ku dzanja la manja la Wanphamvu zonse, akudza ndi mitambo ya kumwamba. "

-Yesu akadzabweranso pa dziko la pansi, sadzabweranso ngati Mpulumutsi koma ngati Olamura.

-Yesu akadzabweranso pa dziko la pansi, adzabwera kudzaŵalamura onse amene sakukhulupilira mwa Iye ngati Mpulumutsi.

-Yesu akadzabweranso pa dziko la pansi, adzaŵatumiza onse amene sakukhulupilira mwa Iye, ku Nyanja Ya Moto Osatha.

-Yesu atamaliza kuŵalamulira ophunzira ache kuti apite pa dziko lonse la pansi kukalalikira Mawu a Mulungu, Iye anabwelera kumwamba.

Tiyeni tiŵerenge Machitidwe a Atumwi 1:10

10-[Ophunzira a Yesu] akuyang'anitsitsa mumlengalenga pamene Iye ankapita, mwadzidzidzi, amuna aŵiri atavara zoyera anayima pambali pawo.

-Kodi amuna aŵiri amene anavala zovala zoyera, amene anayima pambali pa ophunzira a Yesu aja anali ndani?
-Aŵiri mwa angero a Mulungu.

-Kodi angero a Mulunguwo anati chiyani kwa ophunzira a Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Machitidwe a Atumwi 1:11

11-Amenewonso anati, "Amuna a ku Galileya, kodi mukuyimiranji pano ndikumayang'anitsitsa kumwamba? Yesu yemweyu amene watengedwa kuchokera kwa inu kunka kumwamba, adzabweranso ngati m'meme mwamuwonera inu Iye akupita kumwamba."

-Angero anati kuti Yesu adzabweranso pa dziko la pansi.

-Kodi Yesu adzachita chiyani akadzabweranso pa dziko la pansi?
-Kodi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani?



Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:5

5-Ndipo pamene iwo analoŵa m'mandamo, anawona mnyamata atakhala ku mbali ya dzanja la manja, atavala mwinjiro woyera, ndipo iwo anadabwa.

-Azimayiwo atangoloŵa m'mandamo, anawona mngero.

-Kodi mngeroyo anati chiyani kwa azimayiwo?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:6

6-Ndipo iye anati, "Musadabwe: Kodi mukufuna Yesu Mnazarene, amene anapachikidwa? Iye anawuka sali pano; Tawonani pa malo amene anamuyika Iyepo."

-Kodi mngeroyo anati chiyani za Yesu?
-Mngeroyo anati kuti Yesu sanali pamenepo.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanali pamenepo?
-Chifukwa chakuti anali atawuka kuchokera kwa akufa.

-Mngeroyo anati kuti Yesu wawuka kuchokera kwa akufa ngati m'mene Iye ananenera.

-Mngeroyo anaŵawuzanso azimayiwo kuti athamange ndipo akaŵawuze ophunzira a Yesu kuti Yesu wawuka kuchokera kwa akufa.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:7-8

7-"Koma pitani, mukaŵawuze ophunzira ache ndi Peturo, kuti akutsogolereni inu ku Galileya. Kumeneko mukamuwona Iye ngati m'mene anakuwuzirani.
8-Ndipo iwo anaturuka nathawa ku manda akun-

thunthumila ndi kudabwa kwambiri. Ndipo sanamuwuze munthu wina aliyense chifukwa chakuti mantha anaŵagwira.

-Azimayiwo anali ndi mantha kwambiri mwakuti sanaŵawuze ophunzira a Yesuwo poyamba.

-Kenako, Mariya wa ku Magadala, anapita kukaŵawuza ophunzira a Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:9-13

9-Ndipo pamene Yesu anawuka m'mamaŵa pa tsiku loyamba la sabata, anayamba kuwonekera kwa Mariya wa ku Magadala, amene Iye anamuturutsa ziwanda zisano ndi ziŵiri.
10-Iye anapita ndikukaŵawuza iwo amene anali kukhala naye amene anali kulira ndipo achisoni.
11-Ndipo iwowo atamva kuti [yesu] ali moyo ndipo iye wamuwona Iye, sanakhulupilire zimenezi.
12-Ndipo zitatha izi, [Yesu] anawonekeranso m'mawonekedwe ena kwa aŵiri a iwo akuyenda kupita ku miraga.
13-Ndipo iwo anabwelera , nakaŵawuza otsalawo, koma nawonso sanaŵakhulupilire.

-Ngakhale kuti Mariya wa ku Magadala ndiponso amuna aŵiri aja anaŵawuza ophunzira a Yesu kuti Yesu wawuka kuchokera kwa akufa, ophunzira a Yesu sanaŵakhulupilirebe iwo.

-Chomcho, kenako Yesu anawonekera yekha kwa ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:14

14-Kenako Yesu anawonekera kwa ophunzira



siyinathe, ndiye kuti Mulungu Atate sanakamuwukitsa Yesu kuchokera kwa akufa.

-Mulungu anakakhala kuti sanakhutitsidwe ndi malipiro abwino kwambiri a tchimo amene Yesu anapereka, ndiye kuti Iye sanakamuwukitsa Yesu kuchokera kwa akufa.

-Apa pali chitsanzo:

-Munthu wina wache waba ng'ombe ndipo akuyenera kukhala mu ndende kwa chaka chimodzi.
-Chaka chitatha iye akuturutsidwa mu ndende muja.

-Kodi msilikali akamuwonanso munthu uja kunja kwa ndende, angamutumizenso iye ku ndendeko?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti munthuyo anali atakhala kale mu ndende kwa chaka chimodzi ndipo anamaliza kulipira mulandu wakuba ng'ombewo.

-Chifukwa chakuti Yesu analipiliratu pa machimo a anthu onse, Mulungu anamuwukitsa Iye kuchokera kwa akufa.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anang'amba nsaru yotchinga ya mkachisi muŵiri?
-Kuwonetsa kuti palibenso kusiyana pakati pa Mulungu ndi munthu.

-Kodi chifukwa chiyani palibenso kusiyana pakati pa munthu ndi Mulungu?
-Chifukwa chakuti Yesu anamaliza kulipira machimo a anthu onse amene ankatisiyanitsa ife ndi Mulungu.

-Yesu anaturuka magazi ache pofuna kutipulumutsa ife ndiponso kutilipilira machimo athu.

-Pamene Yesu ankafa pa mtanda paja anati kuti, “Kwatha.”
-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?

-Kodi Yesu ankatanthawuza kuti moyo wache watha?
-Ayi.

-Kodi nanga Yesu ankatanthawuza chiyani pa mtanda paja pamene ananena kuti, “kwatha.”

-Yesu ankatanthawuza kuti ntchito yopulumutsa anthu imene Mulungu Atate anamupatsa Iye, yatha.

-Kodi chifukwa chiyani ntchito imene Mulungu Atate anamupatsa Yesu inatha?
-Chifukwa chakuti imfa ya Yesu inalipiliratu machimo a anthu onse.
-Chifukwa chakuti magazi a Yesua analipiliratu machimo a anthu onse.

-Kodi tingadziŵe bwanji kuti ntchito ya Yesu yopulumutsa anthu inatha?
-Chifukwa chakuti imfa ya Yesu inali msembe yabwino kwambiri kwa anthu onse.
-Chifukwa chakuti magazi a Yesu anali msembe yabwino kwambiri kwa anthu onse.

-Kodi tingadziŵenso bwanji kuti ntchito ya Yesu yopulumutsa anthu inatha?
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate anamuwukitsa Yesu kuchokera kwa akufa.

-Ntchito ya Yesu yopulumutsa anthu inakakhala kuti



ache khumi ndi m’modzi akudya chakudya; Iye anaŵadzudzula chifukwa cha kusoŵa kwa chikhulupiliro kwawo ndi kuwuma mtima kwawo, chifukwa sanaŵavomereze iwo amene adamuwona Iye atawuka.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anaŵadzudzula ophunzira ache?

-Chifukwa chakuti iwo sanakhulupilire kuti Yesu wawuka kuchokera kwa akufa.

-Kenako Yesu anaŵapatsa lamulo ophunzira achewo.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 16:15

15-Ndipo [Yesu] anati kwa iwo, “Pitani pa dziko lonse la pansi ndipo mukalalikire Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. “

-Kodi lamulo limene Yesu anaŵapatsa ophunzira achewo linali lotani?
-Linali lakuti apite pa dziko lonse la pansi kukalalikira Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse.

-Kodi Uthenga Wabwino ndi chiyani?
-Mawu a Mulungu.

-Kodi Yesu anapereka lamulo limeneli kwa ophunzira ache okha?
-Ayi.

-Yesu anapereka lamulo limeneli kwa ophunzira ache ndi onse okhulupilira mwa Iye.

-Yesu akufuna kuti anth onse amene akumukhulupilira Iye apite kwa athu ena ndikumakaŵawuza Mawu a Mulungu.

-Ngati m'mene Yesu anaŵakondera anthu onse, Iye akufuna kuti ifenso tiŵapulumutse anthu onse ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:16

16-[Yesu anati], "Pakuti Mulungu anakonda dziko lonse la pansi kotero kuti, anampereka Mwana wache m'modzi yekha, kuti aliyense okhulupilira Iye, asatayike, koma akhale nawo moyo osatha."

-Ichi ndiye chifukwa chimene ine ndabwelera, kudzakuwuzani Mawu a Mulungu.

-Chomcho kuti inu musafe ndikupita ku Nyanja ya Moto ndi chilango chosatha.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anayenera kufa?
-Kodi Yesu anachimwa?
-Ayi,

-Kodi nanga chifukwa chiyani Yesu anayenera kufa?
-Chifukwa chakuti anthu onse achimwa, tiyenera kulipira pa chilango cha Mulungu pa tchimo lathulo.

-Kodi chilango cha Mulungu pa tchimo ndi chiyani?
-Imfa.

-Chifukwa chakuti anthu onse achimwa, malingana ndi kuyera kwa Mulungu, kukutilamura ife kuti tiyenera kulipira tchimo lathu ndi imfa.

-Palibenso njira ina iliyonse yolipilira tchimo lathu kupatula imfa.



-Inde, chifukwa chakuti Mulungu amatikonda ife, Iye sakufuna kuti ife tife.

-Kodi tchimo lathu lingalangidwe bwanji ndi imfa, ife tikadalibe ndi moyo?

-Yesu, Mulungu Mpulumutsi, anafa m'malo mwathu.
-Yesu, Mulungu Mpulumutsi, anafa kuti ife tikhale ndi moyo.

-Izi ndi zimene sankazimvetsa ophunzira a Yesu.

-Sankamvetsetsa kuti Yesu anayenera kufa koma aŵapulumutsabe iwo.

-Iwo sankamvetsetsa kuti imfa ya Yesu yekha ingathe kuŵapulumutsa iwo.
-Imfa ya Yesu pa mtanda inali imfa imene inalipira machimo athu.

-Magazi a Yesu amene anaturuka pa mtanda paja ndi amene analipira machimo athu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anayilandira msembe ya Abele ndikuyikana msemba ya Kayini?
-Chifukwa chakuti Abele anabweretsa magazi a mwana wa nkhosa pamene Kayini sanatero.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapha ana amuna oyamba kubadwa a a Iguputo osakhala a a Isirayeli?
-Chifukwa chakuti a Isirayeli anapaka magazi a mwana wa nkhosa mu zitseko zawo.

-Yesu ndi nkhosa ya Mulungu.
-Mulungu Atate anampereka Yesu ngati msembe ya nkhosa kuti alipire machimo athu.